# CHIMUTU CLUSTER EXAMINATION BOARD

**2024 END OF TERM TWO STANDARIZED EXAMINATION FOR STANDARD 5**

**CHICHEWA**

**(100 MALIKISI)**

**Tsiku: _____ / ____/ 2024** **Nthawi: ______________**

**DZINA LA OPHUNZIRA: ________________________________________________**

(Surname first)

**DZINA LA SUKULU: __________________________________________________**

## GAWO A (30 MALIKISI)

**Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri omwe ali m'munsiwa. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata asachepere 100 koma asapyole 150**

1. Lembani chimangirizo chanu pa mutu uwu '**SUKULU YATHU'**. Tsatani izi polemba

   **Ndime yoyamba**
   - Tchulani dzina la sukulu yanu
   - Ili mdera liti?
   - Pali aphunzitsi angati?

   **Ndime yachiwiri**
   - Tchulani maphunziro omwe mumaphunzira pasukuluyo
   - Nanga inu mumakonda maphunziro ati? Perekani awiri
   - Perekani chifukwa chimene mumakondera maphunziro mwatchulawo

   **Ndime yachitatu**
   - Fotokozani kufunika kwa sukulu pa moyo wanu. Lembani mfundo ziwiri

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa nzanu yomufotokozera za matenda omwe afala m'dera lanu. Mwa zina

   **Ndime yoyamba**
   - Tchulani dzina la matenda omwe afala m'dera lanu
   - Kodi matendawa amafala m'njira yanji?

   **Ndime yachiwiri**
   - Tchulani zizindikiro za matenda omwe m'dera lanu
   - Fotokozani kuopsa kwa matendawa

   **Ndime yachitatu**
   - Fotokozani zomwe mukuchitapo pofuna kuchepetsa kufala kwa matendawa m'dera lanulo

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

________________________________________________

## GAWO B (MALIKISI 20)

3. Kumvetsa nkhani

Nabiyeni adali mwana wa Angozo. Amayi ake adali a Nambewe. Iyeyu adabadwira m'banja la ana asanu ndi awiri, akazi okhaokha. Nabiyeni adali mwana wachisamba m'banjamu.

Makolo ake a Nabiyeni adali osaiyana m'makhalidwe awo. Amayi ake adali okonda kugwira ntchito zapabanjapo. Amakondanso kulima chimanga, mtedza, nyemba komanso chinangwa. Atate ake a Ngozo amakonda kumwa mowa basi.

aNambewe ankawapempha amuna awo kuti asiye kumwa mowa koma iwo amakanitsitsa. Nabiyeni sadapite patali ndi maphunziro chifukwa chosowa thandizo lokwanira.

**Mafunso**

(a) Kodi mayi ake a Nabiyeni adali yani?
_______________________________ malikisi 2

(b) Kodi m'banjali mudali ana angati?
_______________________________ malikisi 2

(c) Tchulani dzina la mwana wa chisamba
_______________________________ malikisi 2

(d) Fotokozani makhalidwe awiri a a Nambewe
_______________________________
_______________________________ malikisi 2

(e) Tchulani mbewu ziwiri zomwe mayiwa amalima
_______________________________
_______________________________ malikisi 2

(f) Ndi khalidwe lotani lomwe bambo Ngozo adali nalo?
_______________________________ malikisi 2

(g) Perekani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi awa
(i) Akazi _______________________________ malikisi 1
(ii) Patali _______________________________ malikisi 1

(h) Perekani tanthauzo la mawu oti '**chisamba**' kuchokera m'nkhani yomwe mwawerengayi
_______________________________ malikisi 2

(i) N'chifukwa chiyani Nabiyeni sadapite patali ndi sukulu?
_______________________________ malikisi 2

(j) Pezani mutu wa nkhani yomwe mwerengayi
_______________________________ malikisi 2

## GAWO C (MALIKISI 5)
## MALONJE

4. Werengani kankhani kotsatiraka ndi kuyankha mafunso otsatirawa

| | | |
|---|---|---|
| Anaphiri | : | Odi! Odi! |
| Adotolo | : | Eee fikani konkuno |
| Anaphiri | : | Mwanayu watentha thupi sitinagone bwino. |

**Mafunso**

(a) Kodi ndi malonje a mtundu wanji mwawerengawa?
_______________________________ malikisi 1

(b) Tchulani yemwe akudwala m'nkhaniyi
_______________________________ malikisi 1

(c) Yemwe akuodila ndi ndani?
_______________________________ malikisi 1

(d) Kodi tikadwala tiyenera kupita kuti?

______________________________________________________________ malikisi 1

(e) Tchulani chizindikiro chimodzi cha matenda a malungo

______________________________________________________________ malikisi 1

## KUPANGA ZIGANIZO (MALIKISI 5)

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa

i. Khola

______________________________________________________________

ii. Masanje

______________________________________________________________

iii. Monyada

______________________________________________________________

iv. Chikhathu

______________________________________________________________

v. Fwafwaza

______________________________________________________________

## GAWO D (MALIKISI 40)

**Mafunso 6 mpaka 10, sankhani mtundu wa mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

6. Mnyamata **<u>akumanga</u>** nyumba
   A. Mfotokozi C. Dzina
   B. Mneni D. mlowammalo
7. Lamiya **<u>ndi</u>** Yohane akupita kumunda
   A. Dzina C. Mfotokozi
   B. Mneni D. Mlumikizi
8. Thokozani wavala Malaya **<u>oyera</u>**
   A. Mfotokozi C. Dzina
   B. Muonjezi D. Mlowammalo
9. **<u>Monica</u>** wapita kusukulu
   A. Mfotokozi C. Dzina
   B. Mneni D. Mperekezi
10. Iwo abwera **<u>mofulumira</u>**
   A. Mneni C. Dzina
   B. Muonjezi D. Mfotokozi

**Mafnso 11 mpaka 13 kutsiriza miyambi**

11. __________ wakale sawawa
   A. Anyezi C. Tsabola
   B. Mchere D. mkaka
12. Chakudza sichiyimba _______
   A. Ng'oma C. Chidebe
   B. Khasu D. Wezulo
13. Kutola ______ ndi m'mawa
   A. Nyemba C. Nkhungudzu
   B. Mzama D. Khobwe

**Mafunso 14 mpaka 15 zilapi**

14. Ndimayesa mphaka koma wakula
   A. Galu C. Mkango
   B. Kambuku D. Njovu
15. Olesani nyama tivinepo ________
   A. Udzudzu C. Mphemvu
   B. Gulugufe D. Ntchentche

**Mafunso 16 mpaka 18 zifanifani**

16. Kukonda m'madzi ngati_________
   A. Bakha C. Chule
   B. Nsomba D. Mvuwu
17. __________ ngati chitedze
   A. Kuyabwa C. Kukoma
   B. Kununkha D. Kukanda
18. Kuda ngati _________
   A. Chikwama C. Nsapato
   B. Mafulufute D. Ntchentche

**Mafunso 19 mpaka 20 lembani mawu amene atsekedwa mzere kunsi kwawo**

19. Iye watenga **<u>chikho</u>**
   A. Zichikho C. Chichikho
   B. Chikho D. Zikho
20. **<u>Mudzi</u>** wakwathu ndiwaukulu
   A. Kumudzi C. Zimudzi
   B. Midzi D. M'midzi

**Mafunso 21 mpaka 23 sankhani chachikazi cha mawu awa**

21. **<u>Abwana</u>** aja afika lero
   A. Ambwana C. Wantchito
   B. Adona D. Akhumutcha
22. **<u>Mkwati</u>** abwera pagalimoto
   A. Mkwatibwi C. Mkamwini
   B. Namwali D. Phungu
23. **<u>Amalume</u>** amakhala ku Lilongwe
   A. Agogo C. Azakhali
   B. Amayi D. Achemwali

**Mafunso 24 mpaka 25 mawu otsutsana m'matanthauzo**

24. Katenge

A. Katule C. Kapereke
B. Kasiye D. Kanyamule

25. Nyoza
    A. Samalira C. Lalatira
    B. Lamulira D. Lemekeza

**Mafunso 26 mpaka 28 tsirizani ziganizo ndi mayina oyenera**

26. _______ yagwera mwana
    A. Mwala C. Nyumba
    B. Mtengo D. Dothi
27. _________ zanga zada kwambiri
    A. Zakudya C. madzi
    B. Nkhuku D. zovala
28. Amalume alima ______ chambiri chaka chino
    A. Mtedza C. Chimanga
    B. Mphepo D. Khobwe

**Mafunso 29 mpaka 30 kalembedwe ka mawu koyenera**

29. **<u>Chosani</u>** ufa unganyowe
    A. Chotsani C. Yanikani
    B. Funsani D. Chotserani
30. Maliya wanyamula **<u>chiseko</u>**
    A. Chitsekero C. Chitseko
    B. Chisenga D. Chivundikiro

**Mafunso 31 mpaka 35 mawu ofanana m'matanthauzo**

31. Nyemba
    A. Mbwanda C. Mzama
    B. Mtedza D. khungudzu
32. Mwano
    A. Khalidwe C. Chipongwe
    B. Mtudzu D. Ulemu
33. Mtoliro
    A. Bonongwe C. Kholowa
    B. Denje D. khanya
34. Chinangwa
    A. Mbatata C. Maungu
    B. Chikhawu D. Mbwani
35. Nkhalango
    A. Dondo C. Thenga
    B. Manda D. Dimba

**Mafunso 36 mpaka 40 sankhani mayina aunyinji**

36. Galu wadya mulu wa nsomba
    A. Wadya C. Galu
    B. Mulu D. Nsomba
37. Amayi anyamula mtolo wa nkhuni
    A. Mtolo C. Timitengo
    B. Nkhuni D. Matsatsa
38. Nkuku wachimanga wapsa
    A. Mkokomo C. Mkuku
    B. Mkoko D. Mkudzi
39. Iye wanyamula mkolo wa nthochi
    A. Mkukuluzi C. Mkuku
    B. Mkoko D. Nthochi
40. Pamsonkhano pali khwimbi la anthu
    A. Namtindi C. Gulu
    B. Khamu D. Khwimbi

**Mafunso 41 mpaka 45 zizindikiro za m'kalembedwe, sankhani ziganizo zomwe zili ndi zizindikiro zoyenera zamkalembedwe**

41.
    A. Ukupita kuti.
    B. Ukupita kuti?
    C. Ukupita, kuti
    D. "Ukupita" kuti?
42.
    A. Ndagula nyemba, tomato, ndi anyezi.
    B. Ndagula nyemba tomato ndi anyezi.
    C. Ndagula nyemba, tomato ndi anyezi.
    D. Ndagula, nyemba tomato ndi anyezi
43.
    A. Juliyasi wadya nsima.
    B. juliyasi wadya nsima.
    C. Juliyasi wadya nsima?
    D. Juliyasi wadya nsima!
44.
    A. Ogo? Ufa uja watayika.
    B. Ogo ufa uja watayika.
    C. Ogo! Ufa uja watayika
    D. Ogo, ufa uja watayika.
45.
    A. M'mudzimu mwangwa zovuta.
    B. M'mudzimu mwagwa zovuta.
    C. M'mudzimu mwagwa zovuta.
    D. M'mudzimu mwagwa zovuta.

**MAFUNSO ATHERA PANO!!!!**